Yesetsani Kuti Muzilambira Mulungu M’njira Yovomerezeka (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m’mutu 16 m’buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* Bukuli likupezekanso pawebusaiti ya jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI KULAMBIRA MULUNGU M’NJIRA YOVOMEREZEKA KUMATANTHAUZA CHIYANI?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena akhoza kunena zotani pa nkhaniyi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Kuti munthu azilambira m’njira yovomerezeka, ayenera kumalambira Yehova yekha.
(Werengani mutu 16 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 1-5.)

Werengani Ekisodo 20:4, 5 ndi 1 Yohane 5:21.

Kodi mavesiwa akusonyeza kuti Mulungu amaiona bwanji nkhani yogwiritsa ntchito mafano pomulambira?

_____

_____

_____

Werengani Deuteronomo 18:10-12.

Kodi mavesiwa akusonyeza kuti Mulungu amaona bwanji kulambira mizimu ya makolo?

_____

_____

_____



Kuchita nawo zikondwerero zachikunja n’kofanana ndi kutola switi yomwe inagwera m’ngalande ya madzi oipa n’kudya

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kuti munthu azilambira m’njira yovomerezeka, ayenera kupewa zikondwerero zilizonse zimene Yehova amadana nazo.

(Werengani mutu 16 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 6-12.)

Werengani Genesis 40:20 ndi Maliko 6:21.

Kodi zimene Baibulo limanena zokhudza zikondwerero ziwiri za kubadwa kwa anthu ena omwe sankalambira Yehova, zikusonyeza chiyani?

Werengani Yesaya 52:11 ndi Aefeso 5:10.

Kodi n’chifukwa chiyani kuganizira mmene maholide achipembedzo anayambira kuli kofunika?

N’chifukwa chiyani muyenera kuyesetsa kulambira Mulungu m’njira yovomerezeka?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Ine *sindilambira* mafano, koma mafanowo amangondithandiza kumva kuti ndili pafupi ndi Mulungu ndikamapemphera.

MUNGAYANKHE KUTI…

N'zosangalatsa kuti mumafuna kuyandikana ndi Mulungu mukamapemphera. Koma kugwiritsa ntchito mafano polambira ndi nkhani yofunika kuiganizira chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Masiku ano anthu sakondwereranso tsiku lobadwa komanso maholide potengera zimene anthu achikunja ankachita, koma imangokhala nthawi yoti munthu asangalaleko ndi banja lake.

MUNGAYANKHE KUTI…

N'zoona kuti munthu ayenera kusangalala ndi banja lake, koma ine ndimaona kuti kuganizira mmene zikondwerero zimenezi zinayambira n'kofunika chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania